

Kabukuka Sabata  
Iliyonse

TRANSLATION  
DEPARTMENT  
(DAWAT-e-ISLAMI)

Kagawo kochokera m'bukhu lotchedwa The Etiquette of Conversation  
lolembedwa ndi Amir Ahl al-Sunnah. وادبنا في الحديث الكوثره kodziwika ndi

# Lankhulani Mokoma Ntima (Gawo 1)



Shaykh al-Tareeqah Ameer Ahl al-Sunnah,  
Muyambitsi wa Dawat-e-Islami, Hazrat Allamah Mawlana  
**Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi** قامشريف  
الرساله

اچھی گفتگو کیجئے (قسط: 1)

## Lankhulani mokoma Ntima (Gawo 1)

### Zankatimu

|                                                                          |   |
|--------------------------------------------------------------------------|---|
| Lankhulani mokoma Ntima (Gawo 1) .....                                   | i |
| <b>Zankatimu</b> .....                                                   | i |
| lankhulani mokoma Ntima (Gawo 1).....                                    | 1 |
| Pemphero la Attar:.....                                                  | 1 |
| Ubwino wonfunira zabwino Mtumiki (Durūd Sharīf) .....                    | 1 |
| kudzudzula malankhulidwe okweza mawu .....                               | 1 |
| Kulankhula mofatsa ndi Sunnah .....                                      | 2 |
| Anthu a chikunja achiruya a mazikweza polankhula mokweza mawu2           |   |
| n'chifukwa chani bulu amalira? .....                                     | 2 |
| Kuyetsemula mokwedza ndi Makrūh .....                                    | 3 |
| Yang'anani Muntu amaene mwakumana naye .....                             | 3 |
| Malankhulidwe a mtumiki ﷺ anali onveka komanso osavuta kunva<br>.....    | 4 |
| Mtumiki wolemekezeka ﷺ amabwereza mawu ake kokwana katatu4               |   |
| Khalidwe m'Malankhulidwe odala a Mtumiki.....                            | 4 |
| Nduna ya Boma imene inalankhula Chirankhulo chovuta<br>(chosanveka)..... | 5 |
| Zinthu ziwiri zime zidzapangitsa Anthu Ambiri kulo ku Gahena .....       | 5 |
| kodi wokhala m'paradiso ndi ndani? .....                                 | 6 |

|                                                                         |    |
|-------------------------------------------------------------------------|----|
| Chitsimikizo cha Paradiso.....                                          | 6  |
| Machimo 80 pa zana iliyonse amachitidwa kuzera pa lilime.....           | 6  |
| Ziwalo zonse zimapempha lilime.....                                     | 7  |
| I'tikāf yapagulu inakhala njira ya kusintha.....                        | 7  |
| Nyumba zapamwamba zachifumu zakuparadiso zowoneka patali.....           | 8  |
| Liwu labwino ndi Sadaqa.....                                            | 8  |
| Kodi Şadaqah ikutanhawuza chani? .....                                  | 9  |
| Amene ali ndi makhalidwe abwino adzakhala pafupi ndi Mtumiki<br>ﷺ.....  | 9  |
| Kodi Makhalidwe abwino ndi chani? .....                                 | 10 |
| Chinthu choopsa kwambiri.....                                           | 10 |
| Khutu lili ngati Galasi ndipo zolankhula zoipa zilingati mwala.....     | 10 |
| Lilime lilibe Fupa .....                                                | 11 |
| Kutchula wina kuti ndi Bulu kapena ndi Nkhumba.....                     | 11 |
| Nditchimo kumuitanira Msilamu ndi maina oipa .....                      | 11 |
| Kutemberera kwa a ngero.....                                            | 12 |
| Nthawi zonse muzilankhula zoona kwa ana.....                            | 12 |
| Mbiri yabwino ya Sayyidunā ‘Abdullāh bin ‘Āmir رَضِيَ اللهُ عَنْهُ..... | 13 |
| Khalani ndi zonse ziwiri Malo komanso ndalama (Nkhani) .....            | 13 |
| Kodi mwana wa Mmuna wosanvera anasintha bwanji? .....                   | 14 |
| Kunamiza ana ndi Malonjezo a bodza.....                                 | 15 |
| Chenjerani posangalatsa ana.....                                        | 15 |

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوَةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى خَاتِمِ النَّبِيِّنَ  
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ ط بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

## lankhulani mokoma Ntima (Gawo 1)<sup>1</sup>

### Pemphero la Attar:

O Inu Ambuye a Muṣṭafā! Aliyense amene awerenge kapena kunvetsera kabuku aka Ka "LANKHULANI MOKOMA Ntima (Gawo 1)", mpatseni mwayi wolankhula motsatira Sunnah, ndipo mukhululukireni iye limodzi ndi makolo ake popanda kuwerengeredwa machimo.

اٰمِيْنُ بِجَاہِ خَاتِمِ النَّبِيِّنَ صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

### Ubwino wonfunira zabwino Mtumiki (Durūd Sharīf)

Mtumiki Womaliza صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Ndithudi, amene adzakhale pafupi ndi ine kwambiri pa Tsiku la Chiweruzo ndi amene amandifunira ine zabwino nthawi zonse."<sup>2</sup>

O inu okonda Mtumiki! Nthawi zambiri munthu amafunika kulankhula, koma kumbukirani kuti kukhala chete n'kwabwino kuposa kulankhula zinthu zololedwa koma zosafunikira.

### kudzudzula malankhulidwe okweza mawu

Allah Wamphanvu zonse akunena m'Qur'an Yopatulika, Gawo 21, Sūrah Luqmān, vesi 19:

---

<sup>1</sup> Mutu uwu watengedwa m'buku lakuti "The Etiquette of Conversation, lolembedwa ndi Ntsogoleri wa Ahl al-Sunnah دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَةِ".

<sup>2</sup> Jami' Tirmidhi, vol. 2, p. 27, Hadith: 484

وَاعْظُضْ مِنْ صَوْتِكَ إِنَّ أَنْكَرَ الْأَصْوَاتِ لَصَوْتُ الْحَمِيرِ ﴿١٩﴾

*ndipo chepetsani mawu anu. Pakuti mawu oyipa kwambiri ndi a bulu.<sup>1</sup>*

## Kulankhula mofatsa ndi Sunnah

Mufti Sayyid Muḥammad Na'im al-Dīn Murādābādī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ walemba m'mafotokozedwe a vesi lodala limeneli: Kupanga phokoso ndikukweza mawu ndi Makrūh (kosayenera) komanso kopanda ubwino. Kulira kwa bulu, ngakhale kuli kokweza, ndi konyansa ndipo kumapangitsa munthu kukhala wosawusika. Mtumiki Wachifundo صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ amakonda kulankhula mofatsa ndipo amadana ndi kulankhula mwa ukali.<sup>2</sup>

## Anthu a chikunja achiruya a mazikweza polankhula mokweza mawu

Allāmah Ismā'īl Ḥaqqī رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ analembe: Anthu akamacheza, mawu oyipa komanso onyansa kwambiri pakati pawo ndi a uyo amene amalankhula mokweza ngati bulu. Anthu achikunja a ku Arabu ankaona kuti kulankhula mokweza ndi chinthu chonyaditsa; vesi ili likutsutsa mchitidwe wawo wodzikuzi umenewu.<sup>3</sup>

## n'chifukwa chani bulu amalira?

Popeza phokoso la bulu latchulidwa, nayi nkhani yophunzitsa pa nkhaniyi. Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati: "Mukanva tambala akulira, pemphani madalitso a Allah chifukwa iwo aona mngelo. Koma mukanva bulu akulira, pemphani chitetezo kwa Allah kuchokera kwa Satana chifukwa iwo aona Satana."<sup>4</sup>

---

<sup>1</sup> Al-Quran, Luqman, vesi 19; kumasulira kwa Kanz al-'Irfān

<sup>2</sup> Tafsir Khazā'in-ul-Irfān, P21, Luqmān, pansa pa Vesi: 19, p. 762

<sup>3</sup> Tafsir Rūh-ul-Bayān, P21, Luqmān, pansa pa Vesi: 19, vol. 7, p. 87, kudusira

<sup>4</sup> Sahih Bukhari, vol. 2, p. 405, Hadith: 3303

Mwachitsanzo: **أَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ**.<sup>1</sup>

## Kuyetsemula mokwedza ndi Makrūh

‘Allāmah Ismā‘īl Ḥaqqī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ analembanso zokhudzana ndi vesi limene latchulidwa kale lija kuti: Izi zikufotokozanso nkhani ya kuyetsemula, kuti kuyetsemula mokweza ndi Makrūh. Choncho, munthu ayesetse kuyetsemula mositsa mawu momwe angathere.<sup>2</sup> Wokondedwa Mtumiki صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati: "Kuyetsemula mokweza kumachokera kwa Satana."<sup>3</sup> Iye صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ sakonda kuyetsemula mokweza mu nzikiti.<sup>4</sup> Allāmah ‘Abd al-Ra‘ūf Munāwī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ akunena za hadith imeneyi kuti: Izi zikutanthauza kuti kuyetsemula mokweza kumadedwa kwambiri m'mzikiti, koma kunja kwa mzikiti.<sup>5</sup>

## Yang'anani Muntu amaene mwakumana naye

Mu gawo 21, Sūrah Luqmān, vesi 18, Allah Wamphanvu zonse walankhula kuti:

**وَلَا تَصْغُرْ خَدَّكَ لِلنَّاسِ**

*Ndipo usatembenezire tsaya lako kumbali polankhulana ndi anthu,*<sup>6</sup>

Allāmah Sayyid Na‘īm al-Dīn Murādābādī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ walemba kuti pakufotokoza vesi: Mukamalankhula ndi anthu, musatembenezire nkhope yanu kumbali powanyoza monga momwe amachitira anthu odzikuza. Chitirani ulemu onse; olemera komanso osauka mwakudzichepetsa.<sup>7</sup> Allāmah Ismā‘īl Ḥaqqī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ writes in Tafsīr Rūh-ul-Bayān: Mukakumana, mukamapatsana moni, kapena mukamalankhulana, onetsani nkhope yanu yonse kwa anthu chifukwa cha

<sup>1</sup> Taisīr Sharh Jāmi' Sagheer, vol. 1, p. 107

<sup>2</sup> Tafsir Rūh-al-Bayān, P21, Luqmān, pansī pa vesi: 19, vol. 7, p. 88, kudusira

<sup>3</sup> Amal-al-Yawm wal-Laylah, p. 119, Hadith: 265

<sup>4</sup> Shu'ab-al-Īmān, vol. 7, p. 32, Hadith: 9356

<sup>5</sup> Fayd-al-Qadeer, vol. 5, p. 311, pansī pa Hadith: 7156

<sup>6</sup> Al-Quran, Luqman, vesi 18; kumasulira kwa Kanz al-'Irfān

<sup>7</sup> Tafsir Khazā'in-al-Irfān, P21, Luqmān, pansī pa vesi: 18, p. 761

kudzichepetsa. Musatembenezire nkhope yanu kumbali kapena kubisa gawo lililonse la nkhopeyo. Ndi chizolowezi cha anthu odzikuza kuyang'ana anthu monyoza, ndipo osauka amawayang'ana mokwiya. Chitirani olemera ndi osauka mofanana ndi khalidwe labwino.<sup>1</sup>

### Malankhulidwe akhale onveka komanso ozindikirika

Pewani kufuwula kapena kulankhula ngati muli pansika, pakuti Mtumiki wa Allah ﷺ sanalankhulepo choncho. Malankhulidwe ake odala sanali okweza kwambiri kapena otsika kwambiri moti wonvetsera amalephera kunva.

### Malankhulidwe a mtumiki ﷺ anali onveka komanso osavuta kunva

wanena kuti Mtumiki Wachifundo ﷺ amalankhula monveka bwino moti wonvetsera aliyense amanvetsa mawu ake odala.<sup>2</sup>

### Mtumiki wolemekezeka ﷺ amabwereza mawu ake kokwana katatu

Kapolo wa Mtumiki, Sayyidunā Anas رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ walankhula kuti nthawi iliyonse imene Mtumiki Wopatulika ﷺ amalankhula, amabwereza mawu ake katatu kuti anveke bwino.<sup>3</sup> Zinalankhulidwa mu Mir'āt-ul-Manājih zokhuza hadith imeneyi: Pofotokoza malamulo, Mtumiki Wokondedwa ﷺ amabwereza nkhani katatu kuti ikhazikike m'maganizo mwa anthu; sizikutanthauza kuti chiganizo chilichonse pofuna kucheza chimabwerezedwa katatu.<sup>4</sup>

### Khalidwe m'Malankhulidwe odala a Mtumiki

Zinalembedwa mu *Şirāt-ul-Jinān*, Volume 7, tsamba 502: Zatchulidwa m'mabuku a Sirah (Mbiri ya Mtumiki) kuti Mtumiki Wopatulika ﷺ samalankhula mopupuluma; m'malo mwake, amalankhula pang'onopang'ono komanso mopumira. Mawu ake anali onveka komanso odziwika bwino, osavuta kunva ndi

---

<sup>1</sup> Tafsir Rūh-al-Bayān, P21, Luqmān, pansa pa Vesi: 18, vol. 7, p. 84

<sup>2</sup> Abu Dawud, vol. 4, p. 343, Hadith: 4839

<sup>3</sup> Sahih Bukhari, vol. 1, p. 52, Hadith: 95

<sup>4</sup> Mir'āt-al-Manājih, vol. 1, p. 194

kuwakumbukira. Ngati nkhani ili yofunika, nthawi zina amabwereza chiganizo katatu kuti onvetsera achigwire bwino. Mtumiki Wankulu komanso Womaliza صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ amapewa kulankhula zachabe ndipo nthawi zambiri amakhala chete. Anapatsidwa chozizwitsa cha Jāmi' Kalimāt, kutanthauza kuti malankhulidwe ake anali achidule koma odzaza ndi tanthauzo lalikulu.

### **Nduna ya Boma imene inalankhula Chirankhulo chovuta (chosanveka).**

Kulankhula kuyenera kukhala kosavuta komanso konveka. Kugwiritsa ntchito mawu ovuta kwambiri kungapangitse anthu kuchita chidwi koma kulephera kupereka uthenga. Invani nkhani iyi kuti munvetsetse nfundoyi: Nthawi ina, Nduna ya Boma yowona za Ulimi wothirira anayendera mudzi wina. Gulu la alimi linabwera kudzakumana naye ndipo linatuma mlimi mmodzi kuti akapemphe chilolezo. Nduna ija inayang'ana m'mwamba ndipo anafunsa kuti: "Tumhari kisht-e-zār par imsāl taqātur-e-amtār huwā ya nahi?" Mlimi wosaphunzira uja atanva chiganizo chimenechi, anatuluka nthawi yomweyo ndipo anauza anzake kuti, "Nduna ya Boma ikuwerenga Quran." Eh! inu okonda Mtumiki! Nduna ija ikanalankhula mofatsa, mlimi uja akananvetsa. Samawerenga Quran; anali malankhulidwe amene anaperekedwa m'njira yovuta kwambiri. Nduna ija imangofunsa ngati kunagwa nvula m'munda chaka chino kapena ayi. Choncho, nthawi zonse mukamalankhula ndi munthu, mukukamba nkhani, kapena mukalemba nkhani kapena buku, yesetsani kugwiritsa ntchito mawu osavuta komanso onveka bwino kwa wonvetsera kapena wowerenga.

### **Zinthu ziwiri zime zidzapangitsa Anthu Ambiri kulo ku Gahena**

Okondedwa abale a Chisilamu! Ndikofunika kwambiri kulamulira lilime. Anthu osawerengeka adzalowa m'Gehena chifukwa cha malilime awo okha. Sayyidunā Abū Hurayrah رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ akunena kuti: Mtumiki Wopatulika صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anafunsidwa kuti kodi ndi ntchito iti imene idzapangitse anthu ambiri kulowa m'Paradiso?' Iye صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati kuopa Allah komanso makhalidwe abwino.'

Kenako anafunsidwa kuti, ‘Kodi n’chani chidzapangitsa anthu ambiri kupita ku Gehena?’ Iye ﷺ anati, ‘Zinthu ziwiri: lilime komanso maliseche.’<sup>1</sup>

## kodi wokhala m’paradiso ndi ndani?

Sayyidunā Abū Hurayrah رَضِيَ اللهُ عَنْهُ akusimba kuti Mtumiki Wopatulika ﷺ anati: Munthu amene Allah Wamphanvu zonse an’teteza kukuipa kwa zimene zili pakati pa nsagwada zake (lilime) ndi zimene zili pakati pa miyendo yake (maliseche) adzalowa m’Paradiso.<sup>2</sup>

## Chitsimikizo cha Paradiso

Munthu amene amateteza kamwa komanso maliseche—kutanthauza kuti, sazigwiritsa ntchito mosemphana ndi Shari’ah—ndi wokhala m’Paradiso. Mnzake wa Mtumiki, Sayyidunā Sahl bin Sa’d رَضِيَ اللهُ عَنْهُ akunena kuti Mtumiki Wokondedwa ﷺ anati: Aliyense amene anganditsimikizire chiyero cha chimene chili pakati pa nsagwada zake ndi chimene chili pakati pa miyendo yake, ine ndidzam’tsimikizira Paradiso.<sup>3</sup> Izi zikutanthauza kuti lonjezo la Paradiso lidzaperekedwa kwa uja amene amateteza lilime lake komanso maliseche ake ku zinthu zimene zinaletsedwa ndi Shari’ah.

## Machimo 80 pa zana iliyonse amachitidwa kuzera pa lilime

Chimene chili pakati pa nsagwada ziwiri chimatanthauza lilime ndi mkamwa, pomwe chimene chili pakati pa miyendo chimatanthauza maliseche. Choncho, munthu ayenera kuteteza lilime lake ku mabodza, miseche, komanso malankhulidwe osaloledwa; kuteteza mkamwa mwake ku zakudya zosaloledwa; komanso kuteteza maliseche ake ku chigololo. Amene akwanitsa zimenezi mosakayikira ndi wolungama. Kumbukirani kuti machimo ambiri amachitika kudzera m’lilime. Amene amateteza lilime lake sadzachita umbala, kapena kupha munthu. Anthu amachita upandu pambuyo poganiza zonama ngati atagwidwa, kunena kuti, Ine ndidzatsutsa. Kunama ndi muzu wa machimo onse. Chitsimikizo

---

<sup>1</sup> Sunan Ibn-e-Mājah, vol. 4, p. 489, Hadith: 4246

<sup>2</sup> Jam’i Tirmidhi, vol. 4, p. 184, Hadith: 2417

cha Mtumiki Wankulu ﷺ chimenechi ndi cha anthu onse mpaka Tsiku la Chiweruzo, ndipo chitsimikizo cha Mtumiki Wachifundo ﷺ ndi chitsimikizo cha Allah Wamphanvu zonse.<sup>1</sup>

## Ziwalo zonse zimapempha lilime

Sayyidunā Abū Saʿīd Khudrī رَضِيَ اللهُ عَنْهُ akunena kuti Mtumiki Wopatulika ﷺ anati: "Munthu akadzuka m'mawa, ziwalo zake zonse zimadzipereka modzichepetsa ku lilime, kunena kuti, 'Opani Allah kukhudzana ndi ife, chifukwa ife tili m'manja mwanu. Ngati inu mukhala olungama, ifenso tikhala olungama; koma ngati inu mukhala opotoka, ifenso tikhala opotoka.'<sup>2</sup>

## I'tikāf yapagulu inakhala njira ya kusintha

Okondedwa abale a Chisilamu! Ngati tigwiritsa ntchito lilime moyenera, ubwino wake ukafika ku chiwalo chilichonse cha thupi. Ngati lapatuka, mwachitsanzo, potukwana wina, lilime likhoza kunva kapena kusanva kupweteka, koma thupi lonse lidzalangidwa chifukwa cha zimenezo. Kuti mukhale ndi chidwi choyang'anira lilime lanu, khalani olumikizana chikhalidwe cha uzimu cha Dawat-e-Islami. Ngati Allah Wamphanvu zonse akupatsani mwayi, pezani ulemu wochita I'tikāf pa mwezi wa Ramaḍān limodzi ndi okonda Mtumiki. ﷺ! Nayi nkhani ya Madani yosonyeza madalitso a I'tikāf. Malinga ndi zimene ananena m'bale wina wa Chisilamu wochokera m'boma la Mandi Bahauddin (Punjab), asanalowe mchikhalidwe cha Dawat-e-Islami, anali m'chizolowezi cha mankhwalu osokoneza bongo komanso mowa. Chizolowezi chake chinakhala choopsa kwambiri moti anafika mpaka pakuba kuti agule mankhwalawo. Izi zinapangitsa kuti banja lake komanso dera lonselo kukhala osasangalala.

Ulendo wake wofuna kusintha unayamba pamene anadalitsidwa pochita I'tikāf limodzi ndi okonda Mtumiki m'mwezi wodala wa Ramaḍān. Pa nthawi ya I'tikāf, anasangalala kukhala m'gulu la anthu olungama ndipo anaphunzira buku la

<sup>1</sup> Mir'āt-al-Manājih, vol. 6, p. 447, ndiyosinthidwa

<sup>2</sup> Jami' Tirmidhi, vol. 4, p. 183, Hadith: 2415

"Faizān-e-Sunnat". Patapita nthawi, anapita ku nsonkhano wa Dawat-e-Islami womwe unachitikira ku Madani Markaz Faizān-e-Madinah ku Mandi Bahauddin. Kuona chiwerengero chachikulu cha okonda Mtumiki atavala kavalidwe ka Chisilamu kunakhudza ntima wake kwambiri. Sabata yotsatira, anapitanso ku nsonkhanowo, ndipo nkhani yochokera pansi pa ntima yomwe inakambidwa inamukhudza kwambiri moti analapa machimo ake ndipo anabwerera kwawo atasintha. Sanayambe kupemphera mapemphero asanu a tsiku ndi tsiku okha, komanso anakulitsa ndevu za kutalika kwa chikhatho, ndipo anayamba kuvala zovala za Sunnah. **اَلْعَبْدُ لِلّٰهِ**. Anapatsidwanso mwayi woyenda ndi Qafilah pofuna kufalitsa uthenga wa chilungamo.

**صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْبِ      صَلَّی اللّٰهُ عَلَی مُحَمَّدٍ**

## Nyumba zapamwamba zachifumu zakuparadiso zowoneka patali

Zinalankhulidwa ndi Khalifa wachinayi wa Chisilamu, Sayyidunā ‘Alī b. Abī Ṭālib **رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ** kuti Mtumiki Wachifundo **صَلَّی اللّٰهُ عَلَیْهِ وَآلِہٖ وَسَلَّم** anati: "M'Paradiso muli nyumba zapamwamba zomwe kunja kwake kumawonekera nkati, ndipo nkati mwake mumawonekera kunja." M'bedwini wina anafunsa kuti: "Inu Mtumiki wa Allah **صَلَّی اللّٰهُ عَلَیْهِ وَآلِہٖ وَسَلَّم**! Kodi zimenezi ndi za ndani?"

Mtumiki Wankulu **صَلَّی اللّٰهُ عَلَیْهِ وَآلِہٖ وَسَلَّم** anayankha kuti: "Ndi za uja amene amalankhula mokoma ntima, amadyetsa ena, amasala nthawi zonse, ndipo amapemphera usiku pamene anthu ali n'tulo."<sup>1</sup>

## Liwi labwino ndi Sadaqa

Kunena chinthu chabwino n'kwabwino kuposa kukhala chete, ndipo kukhala chete n'kwabwino kuposa kulankhula zachabe. Kunena chinthu choipa ndi koipa, koma mawu abwino ndi Ṣadaqah. Sayyidunā Abū Hurayrah **رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ** akunena kuti

---

<sup>1</sup> Jami' Tirmidhi, vol. 3, p. 396, Hadith: 1991

Mtumiki Wopatulika **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم** anati: "liwu labwino ndi Şadaqah.<sup>1</sup>

### Kodi Şadaqah ikutanthawuza chani?

'Sadaqah' ikutanthauza kulandira mphotho ya sadaka. Mtumiki Wankulu komanso Womaliza **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم** anati: "Ntchito iliyonse yabwino ndi Şadaqah.<sup>2</sup>

**Kufotokozero:** Izi zikutanthauza kuti Şadaqah simathera pa kupereka chuma kokha, koma ntchito iliyonse ngakhale yaing'ono yabwino, ngati itachitika ndi ntima wonse, amalandira mphotho ya sadaka. Izi zikuphatikizapo kulankhula mokoma ntima komanso mofatsa kwa m'bale wako wa Chisilamu.<sup>3</sup>

### Itanirani kuzabwino mwa nsanga

Musabise upangiri uliwonse wopindulitsa, podziwa kuti onvetsera angafunike nsonkhano wina kuti anvetse; m'malo mwake, ufotokozeni mokwanira popanda kuchedwa. Musanene kuti, "Ndidzakuuzani zinazo pambuyo pake, pakuti palibe chitsimikizo chakuti wolankhula kapena wonvetsera adzakhala ndi moyo mpaka nsonkhano wotsatira.<sup>4</sup>

### Amene ali ndi makhalidwe abwino adzakhala pafupi ndi Mtumiki ﷺ

Mnzake wa Mtumiki, Sayyidunā Jābir **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم** akunena kuti Mtumiki Wachifundo **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم** anati: "Ndithudi wokondedwa kwambiri pakati panu kwa ine komanso amene adzakhala pafupi nane kwambiri pa Tsiku la Chiweruzo adzakhala iwo amene ali ndi makhalidwe abwino kwambiri. Odedwa kwambiri pakati panu kwa ine komanso amene adzakhala patali kwambiri ndi ine pa Tsiku la Chiweruzo adzakhala iwo amene ali ndi makhalidwe oipa, amene amalankhula mopitirira muyezo, olankhula mwamwano, komanso amene amadzaza nkamwa

<sup>1</sup> Sahih Bukhari, vol. 2, p. 306, Hadith: 2989

<sup>2</sup> Sahih Bukhari, vol. 4, p. 105, Hadith: 6021

<sup>3</sup> Mir'āt-al-Manājih, vol. 3, p. 95

<sup>4</sup> Islāh-e-A'māl, p. 360; Al-Hadeeqah al-Nadiyyah, vol. 1, p. 95

mwawo akamalankhula.<sup>1</sup>

## Kodi Makhalidwe abwino ndi chani?

Mufti Aḥmad Yār Khān رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ akufotokoza hadith imeneyi motere: Munthu amene ali ndi makhalidwe abwino nthawi zambiri amachita ntchito zambiri zolungama ndipo amachita machimo ochepa. Kuona ntima (kutanthauza, kukhulupirika, kukwaniritsa malonjezo, komanso chilungamo m'machitidwe, ndi zina zotero) zonsezi zikuphatikizidwa m'makhalidwe abwino. Anthu okhala ndi makhalidwe oipa nthawi zambiri amachita ntchito zoipa. Makhalidwe oipa mwa iwo okha ndi tchimo komanso ndi gwero la machimo ena ambiri. Kunama, kusakhulupirika, kuswa malonjezo, komanso chinyengo m'zamalonda zonsezi ndi nthambi za makhalidwe oipa.<sup>2</sup>

## Chinthu choopsa kwambiri

O Inu okonda Mtumiki! Kuteteza lilime n'kofunika kwambiri, pakuti katangale ndioyipa kwambiri zimachokera mwa ilo. Mnzake wa Mtumiki, Sayyidunā Sufyān bin ‘Abdullāh رَضِيَ اللهُ عَنْهُ akusimba kuti: Nthawi ina ndinafunsa Mtumiki kuti, ‘Inu Mtumiki wa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ! Kodi n'chani chimene mukuona kuti ndi choopsa kwambiri komanso choipa kwambiri kwa ine?’ Mtumiki Wopatulika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anagwira lilime lake lodala ndipo anati: ‘Ichi.’<sup>3</sup>

## Khutu lili ngati Galasi ndipo zolankhula zoipa zilingati mwala

‘Allāmah ‘Abd al-Wahhāb Sha‘rāni رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anati: Ndinamunva Shaykh Afdal-ud-Dīn رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ akunena kuti khutu lili ngati galasi, ndipo zolankhula zoipa zili ngati miyala. Nthawi zonse miyala ikaponyedwa pa galasi, limasweka kukhala tizidutswa-dutswa.<sup>4</sup>

---

<sup>1</sup> Shu'ab al-Īmān, vol. 6, p. 234, Hadith: 7989

<sup>2</sup> Mir'āt-al-Manājih, vol. 6, p. 436, kudutsira

<sup>3</sup> Jami' Tirmidhi, vol. 4, p. 184, Hadith: 2418

<sup>4</sup> Al-Minan-al-Kubrā, p. 547

## Lilime lilibe Fupa

Zinanenedwa kuti: "Lilime lilibe fupa, komabe limaswa mafupa. Lilime si lupanga, komabe limakhetsa magazi. Munthu wina ananena mokongola kuti: "Nkhani zimene anthu amakangana mpaka kuikidwa mmanda pansi pa matani a nthaka zisanu ndi imodzi ndi nkhani zomwezo zomwe, ngati munthu akafuna kungozikwirira ndi fumbi pang'ono (kutanthauza kuzinyalanyaza, kuzisiya), zikanamulola kukhala ndi moyo wantendere m'dziko lino."

## Kutchula wina kuti ndi Bulu kapena ndi Nkhumba

Nkulu yemwe ndi Tābi'i, Sayyidunā Ibrāhīm Nakha'ī رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ, akunena kuti: "Ngati munthu atchula wina kuti ndi bulu kapena Nkhumba, adzafunsidwa pa Tsiku la Chiweruzo: 'Ndiuze! Kodi Ine ndinawapanga kukhala bulu? Ndiuze! Kodi Ine ndinawalenga kukhala Nkhumba?'"<sup>1</sup>

## Nditchimo kumuitanira Msilamu ndi maina oipa

Inu okonda Mtumiki! Kutchula Nsilamu dzina loipa ndikoletsedwa ndi lamulo la Qur'an. Allah Wamphanvu zonse akunena m'Qur'an Yopatulika, Gawo 26, Sūrah al-Hujurāt, vesi 11:

وَلَا تَتَابَرُؤْا بِالْأَلْقَابِ ط

*ndipo musatchulane mayina onyozana.*<sup>2</sup>

Choncho, ndikoletsedwa kumpatsa Msilamu dzina loipa. Akatswiri omasulira Quran afotokoza vesi ili m'njira zosiyanasiyana. Nawa mafotokozedwe awiri kuchokera mu Şirāt-ul-Jinān:

1. Akatswiri ena amati zimatanthauza kutchula Msilamu kuti ndi galu, bulu, kapena nkhumba.

<sup>1</sup> Ihyā al-'Ulūm, vol. 3, p. 200; Ihyā ul-'Ulūm (Urdu), vol. 3, p. 494

<sup>2</sup> Al-Quran, Al-Hujurat, verse 11; kumasulira kuchokera mu Kanz al-'Irfān

2. Ena anati zimatanthauza kugwiritsa ntchito dzina lililonse limene likutanthauza kunyozeka kwa Msilamu ndipo iye akudana nalo. (Komabe, mayina aulemu amene ali oona, monga dzina la Sayyidunā Abū Bakr kukhala ‘Atīq, Sayyidunā ‘Umar kukhala Fārūq, Sayyidunā ‘Uthmān kukhala Dhū al-Nūrān, Sayyidunā ‘Alī kukhala Abū Turāb, ndipo Sayyidunā Khālid kukhala Sayfullāh.) Mayina amene akhala mayina odziwika ndipo sakudedwa ndi amene amatchulidwawo alinso oloedwa, monga A‘mash (wofooka maso) ndi A‘raj (wolumala mwendo mmodzi), amene onse anali akatswiri odziwika a ma Hadith.<sup>1</sup>

### Kutemberera kwa a ngero

Mtumiki Womaliza Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Aliyense amene atchula Msilamu dzina lina kuposa lake (kutanthauza dzina loipa), angelo amamutemberera.<sup>2</sup> **Kufotokozero:** Allāmah ‘Abd al-Ra‘ūf Munāwī رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْهِ (d.1031 AH) analongosola: (Tanthauzo la angelo amamutemberera ndi lakuti) angelo amapemphera kuti munthu wotereyo alandidwe ulemu ndi udindo wa olungama. Kutchula wina kudzera m'dzina lina osati lake kungatanthauze kugwiritsa ntchito mayina kapena udindo umene iye amadana nawo. Komabe, palibe vuto ngati munthu atchulidwa ndi mawu amene sakudedwa, monga "Inu ‘Abdullāh!" kapena "Inu m'bale!" m'malo mwa dzina lawo lenileni.<sup>3</sup>

### Nthawi zonse muzilankhula zoonā kwa ana

Sahabi wa Mtumiki, Sayyidunā ‘Abdullāh bin ‘Āmir رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ Analankhula kuti (pokumbukira zimene zinachitika mu umwana wake): Mtumiki Wopatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali panyumba pathu tsiku lina pamene amayi anga anandiitana, kunena kuti, ‘Bwera kuno, ndikupatse kanthu. Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anafunsa amayi anga kuti, ‘Kodi mufuna kumupatsa chani?’ Iwo anayankha kuti,

<sup>1</sup> Tafsir Khāzin, P26, Al-Hujurāt, pansa pa vesi: 11, vol. 4, p. 170

<sup>2</sup> Jāmi' Sagheer, p. 525, Hadith: 8666

<sup>3</sup> Fayd al-Qadīr, vol. 6, p. 163, pansa pa Hadith: 8666,

‘Ndifuna kumupatsa chipatso cha tende.’ Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, ‘Muja simukanamupatsa kalikonse, bodza limodzi likanalembedwa pa inu.’<sup>1</sup>

### Mbiri yabwino ya Sayyidunā ‘Abdullāh bin ‘Āmir رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ

Tiyeni tiphunzire za moyo wodala wa Sayyidunā ‘Abdullāh bin ‘Āmir رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ, amene analandira hadith imeneyi. Dzina lake ndi ‘Abdullāh ibn ‘Āmir ibn Kurayz. Iye ndi wochokera ku Quraysh, ndipo ndi nsuweni wa Khalifa Wa chitatu wa Chisilamu, Sayyidunā ‘Uthmān b. ‘Affān رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ. Atabadwa, anatengedwa kupita kwa Mtumiki Wopatulika صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ, amene anamudalitsa po uzira. Anatumikira monga kazembe wa ku Basra ndi Khurasan pa nthawi ya Ukhulufa wa Sayyidunā ‘Uthmān رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ. Sayyidunā Amīr Mu‘āwiyah رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ anamusungabe pa udindo umenewu. Anali iye amene anakumba ngalande ya ku Basra, ndipo amadziwikanso ndi kuwolowa manja kwake. Anamwalira m’chaka cha 57 kapena 58 AH.<sup>2</sup>

### Khalani ndi zonse ziwiri Malo komanso ndalama (Nkhani)

Sayyidunā ‘Abdullāh bin ‘Āmir رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ nthawi ina anagula malo a pansika a nkulu yemwe ndi Tābi‘ī, Sayyidunā Khālid bin ‘Uqbah رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ pa ntengo wa 70 kapena 80 thousand Dirhams. Patapita nthawi usiku umenewu, ananva kulira kochokera m'nyumba ya Sayyidunā Khālid ndipo anafunsa banja lake kuti, "N'chifukwa chani akulira?" Iwo anayankha kuti, "Chifukwa nyumba yagulitsidwa." Kenako anauza kapolo wake kuti, "Inu kapolo! Pita kwa Sayyidunā Khālid bin ‘Uqbah ndipo ukamuuze kuti: Sungani nyumbayo komanso ndalama zimene tinagwirizana zija."<sup>3</sup> Chifundo cha Allah Wamphanvu zonse chikhale pa iwo, ndipo ifenso tikhululukidwe popanda kuwerengeredwa ntchito zathu chifukwa cha iwo.

أَمِينُ بَجَاهِ خَاتِمِ النَّبِيِّينَ صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

<sup>1</sup> Abu Dāwūd, vol. 4, p. 387, Hadith: 4991

<sup>2</sup> Al-Iṣābah li Ibn Ḥajar, vol. 5, pp. 14-15

## Kodi mwana wa Mmuna wosanvera anasinthwa bwani?

Kuti mukulitse chikondi chanu pa masahaba a Mtumiki komanso Ahl al-Bayt رَضِيَ اللهُ عَنْهُمْ, komanso kuti mukhale ndi malingaliro olemekiza mayina a Asilamu, komanso kuti mukhale ndi chizolowezi cholankhula zoonza nthawi zonse ngakhale kwa ana, khalani woyenda m'ma Qafilah a Dawat-e-Islami. Invani ndipo sangalalani ndi nkhanu iyi ya Madani ya momwe mwana wosanvera anasinthira kudzera m'madalitso a chikhalidwe cha Dawat-e-Islami: Mnyamata wina wochokera ku Jhang, Punjab, nthawi ina anali wonyalanyaza mapemphero komanso wosanvera makolo ake, motero amaphwanya ufulu wa Allah Wamphanvu zonse komanso ufulu wa zolengedwa zake. Tsiku lina, wachibale wina wolumikizidwa ndi Dawat-e-Islami anachezera sitolo ya abambo ake, pomwe mnyamata uja analiponso. M'bale wa Chisilamu uja anamuitana kuti adzakhale nawo pa nsonkhano wa pa sabata wa Dawat-e-Islami wolimbikitsa Sunnah, umene anavomereza ndipo anapitako Lachinayi. Anapeza ntendere wa uzimu pamenepo moti kupitako Lachinayi lililonse kunakhala chizolowezi chake. Kudzera n'kulalikirira kwa m'bale wa Chisilamu uja, anadalitsidwanso poyenda n'Qafilah yamasiku atatu pofuna kuphunzira Sunnah. Pa nthawi ya Qafilah, okonda Mtumiki anamulimbikitsa kuti alembetse maphunziro ophunzitsidwa. Atabwerera kwawo, anachita manyazi chifukwa cha kusanvera kwake kwa makolo ake. Atakhala pamapazi awo, analira ndipo anapempha chikhululukiro, chifukwa cha chikondi, anamukhululukira. Kenako ana wa uza kuti, "Moyo ndi waufupi kwambiri, ndipo palibe amene akudziwa kuti udzatha liti. Ndikufuna kupeza chidziwitso cha chipembedzo ndili ndi moyo. Ndi mawu otere,

anatsimikizira makolo ake kuti amulole kulowa nawo maphunziro awo. Atalandira chilolezo, anasonkhanitsa katundu wake mosangalala ndipo anatenga nawo mbali pa maphunzirowo, kumene anaphunzira zambiri. Moyo wake unasintha kwambiri moti uja yemwe nthawi ina samanvera makolo ake tsopano amapsompsona mapazi awo asanachoke panyumba. Patapita nthawi, anamaliza maphunziro a Farḍ 'Ulūm (Chidziwitso Chofunikira cha Chisilamu) ndipo pamapeto pake anapatsidwa udindo woyang'anira UC Mashawarat m'dongosolo la Dawat-e-Islami. Allah

Wamphanvu zonse am'patse iye komanso ife kukhazikika m'makhalidwe odala a Dawat-e-Islami.

اٰمِيْنُ بِجَاهِ خَاتِمِ النَّبِيِّينَ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

صَلُّوْا عَلٰى الْحَبِيْبِ صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّدٍ

## Kunamiza ana ndi Malonjezo a bodza


Nkulu yemwe ndi Tābi'ī, Sayyidunā Imām Mujāhid رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْهِ anati: Mawu aliwonse amene munthu amalankhula amasungidwa (m'buku lake la ntchito), ngakhale pamene auza mwana wake kuti akhale chete ndidzakugulira zakuti-zakuti (pamene iye alibe cholinga chochita zimenezo) amalembedwa kukhala wabodza.<sup>1</sup>

## Chenjerani posangalatsa ana

Tsoka ilo, masiku ano, mabodza amauzidwa pafupipafupi pofuna kusangalatsa ana. Mwachitsanzo, popanda cholinga chenicheni, anthu amati: "Tidzakugulirani zidole, zende, masiwiti, mabisiketi akuti-akuti; tidzakuphikirani ndipo tidzakudyetsani chakudya chakuti-chakuti; tidzakutengerani kumalo akuti-akuti kukacheza," ndi zina zotero. Mbuye wathu owona ntima, chifukwa cha Mtumiki wanu oona ntima صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ, tipatseni mwayi wolankhula zoona nthawi zonse.

اٰمِيْنُ بِجَاهِ خَاتِمِ النَّبِيِّينَ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

<sup>1</sup> Ihyā al-'Ulūm, vol. 3, p. 142; Ihyā ul-'Ulūm (Urdu), vol. 3, p. 350



Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran  
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan.

UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 1262

Web: [www.dawateislami.net](http://www.dawateislami.net) | E-mail: [translation@dawateislami.net](mailto:translation@dawateislami.net)